


KUKULA MU DONGOSOLO LA MULUNGU



BUKU LA ANA

KUKULA MU DONGOSOLO LA MULUNGU

BUKU LA ANA

CSS- 01- 98

ZA MKATIMU

PHUNZIRO

TSAMBA

1.	YESU NDI APHUNZITSI	1
2.	PAULO BWENZI LA TIMOTEO	4
3.	PAULO NDI LIDIYA	7
4.	SAMUELI ATHANDIZA	10
5.	YESU APHUNZITSA ZA CHISAMALIRO CHA MULUNGU	13
6.	ULENDO WA YAKOBO	16
7.	MAFUNDE AKULU	19
8.	MMENE KAZEMBE NAMANI AMADWALA	22
9.	CHAKUDYA CHABWINO CHA DANIELI	25
10.	MMENE KHOMA LINAMANGIDWIRA	28
11.	PHOSO LA MNYAMATA	31
12.	DAVIDE NDI MUNTHU WOPUNDUKA	34
13.	MSAMARIYA WABWINO	37

PHUNZIRO 1.

YESU NDI APHUNZITSI

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Luka 2:40- 52.

MAWU A PAMTIMA:

"... Tiyezi ku nyumba ya Yehova."

(Masalmo 122:1)

Yesu anamva phokoso la m'mamawa. Namvanso fungo la buledi. Iye anauka nakhala tsonga napukuta m'maso mwake. Ndipo Iye anakumbukira kuti, lero ndi tsiku lapadera, chifukwa iye anali kupita pa ulendo ndi Mariya ndi Yosefe. Iye anali kupita ku Kachisi wamkulu ku Yerusalemu.

Yesu anadzuka mwamsanga, nayalula mphasa yake nayamba kuthandiza Mariya kuika buledi ndi nsomba mu dengu. Tsono inafika nthawi kuti ayambe ulendo wao wautali.

Mabanja ena ambiri anapitanso ku Yerusalemu. Iwo onse anayendera pamodzi. Mariya anali pa tsogolo ndi akazi anzake. Iwo anali wokondwa pomakambirana ndi kucheza. Yosefe anatsatira pambuyo ndi amuna anzake. Yesu anali kuyendanso ndi atsikana ndi anyamata anzake. Iwo anali kuyenda uku akuyimba nyimbo zawo. Nthawi zina ana anali kumathyola maluwa. Pa nthawi ya usiku banja lirilonse linali kudzimangira msasa mbali mwa mseu.

Pomaliza m'modzi wa iwo anaitana anzake nati, "Ndaona Kachisi."

Yesu anafulumira kuti akaone Kachisiyo. Naona kuti anali okongola kopambana. Iye anayenda mmiseu ndi anthu ena, nakwera pa makwerero a Kachisiyo. Yesu anali kumvetsera nyimbo zapadera zachilemekezo zimene zinali kuimbidwa. Iye anali kumvetseranso m'mene aphunzitsi anali kuwerenga mpukutu wa Buku Lopatulika. Iye anafunsa mafunso. Iye anamvetseranso zonse zimene aphunzitsi anali

kuphunzitsa. Yesu anali wokondwa kopambana.

Posachedwa inakwana nthawi yakuti adzibwerera kwawo. Mariya ndi Yosefe ndi abwenzi awo anayamba ulendo wawo. Iwo anayenda m'miseu ya mumzindamo, mpaka anaturukira kunja kwa mzindawo nayamba kuyenda m'miseu ya dothi.

Kutada mabanja onse anasonkhana pamodzi kudya ndi kugona. Mariya anafunsa Yosefe kuti, "Bambo, nanga Yesu ali kuti?" Yosefe anati, "Ine ndimayesa ali ndi inu?" Pamenepo anayamba kufunsa abwenzi awo kuti, "Kodi mwamuona Yesu?" Koma onse anakana nati, "Sitinamuone."

Mariya ndi Yosefe anathamangiranso ku Yerusalemu. Iwo anazungulirazungulira m'miseu yonse. Nafunsa aliyense amene anakomana nawo kuti, "Kodi simunationere mnyamata wa zaka khumi ndi ziwiri?" Koma palibe m'modzi anadziwa kumene kunali Yesu.

Pomaliza Mariya ndi Yosefe anapita ku Kachisi. Iwo anakwera pamakwerero wolowa m'Kachisimo. Ndipo taonani, Yesu anali m'menemo. Anali kulankhula ndi aphunzitsi. Iye sanadziwe kuti nthawi yopita kwawo yakwana.

Yesu anatsazika aphunzitsi, pamenepo anapita kwawo pamodzi ndi Mariya ndi Yosefe.



"...Tiyeni kunyumba ya Yehova."

(Masalmo 122:1)

PHUNZIRO 2.

PAULO BWENZI LA TIMOTEO

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Machitidwe 16:1- 3.

MAWU A PAMTIMA:

"Bwenzi limakonda nthawi zonse..."

(Miyambo 17:17)

Timoteo anakonda kupita ku tchalichi. Iye anakonda kuona abwenzi ake aku tchalichi. Iye anakondanso kumva mlaliki akuwerenga Buku Lopatulika. Timoteo anadziwa ndime zambiri za m'Buku Lopatulika. Nthawi zina mlaliki anali kuwerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene Timoteo anaziphunzira.

Tsiku lina mlaliki watsopano anadza ku tchalichi cha Timoteo. Dzina lake anali Paulo.

Timoteo anamvetsera mwa kaso m'mene Mlaliki Paulo anali kulankhula. Iye anati, "Mulungu anatumiza Mwana wake. Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Yesu amakukondani. Iye anafuna kuti inunso mumkonde. Mlaliki Paulo anauza anthu zinthu zambiri za Yesu.

Ataturuka mapemphero mlaliki Paulo anapita ku nyumba kwa Timoteo. Iye anali kukambirana ndi mai a Timoteo, Yunesi. Iye anachezanso ndi Ambuye ake a Timoteo, Loisi. Iye anawauza iwo za bwenzi lake Yesu. Nati, "Yesu ndi bwenzi lanunso," ndipo Timoteo anati, "Ndikukondwera kuti Yesu ndi bwenzi langa." Mai Yunesi ndi Agogo Loisi anali okondweranso. Iwo anapempha mlaliki Paulo kuti adzabwerenso kudzacheza nawo.

Mlaliki Paulo anakacheza kunyumba kwawo nthawi zambiri. Nthawi zina anali kukadya nawo komweko. Nthawi zina anali kukangocheza. Timoteo anakonda kumva za Yesu.

Tsiku lina Mlaliki Paulo anachoka kumudzi wa Timoteo, nati, "Ndiyenera kupita kumidzi ina. Ndiyenera kukawauzanso ena za Yesu. Tsiku lina ndidzabweranso kudzakuonani."


Timoteo anagwira ntchito, masewera, ndi kumaphunzitsa. Iye anakulakulabe. Pomaliza anali munthu wachikulire.

Tsiku lina Mlaliki Paulo anabwereranso kumudzi kwa Timoteo, nafika kunyumba ya Timoteo. Timoteo anali wokondwa kwambiri. Iye anakambirana ndi Paulo za bwenzi lawo Yesu. Paulo anamuuza za malo amene anakachezera. Iye anamuuzanso za anthu amene anavomereza kukonda Yesu.

Paulo anafunsa Timoteo kuti, "Kodi sufuna kukhala mthandizi wanga?" Timoteo anayankha kuti, "Inde ndingakondwere kukhala mthandizi wanu. Ndingakhale okondwa kuuza anthu ena za Yesu."

Timoteo ndi Paulo anapita kumidzi ina pamodzi. Iwo anauza Amai ndi Abambo za Yesu. Iwo anauzanso anyamata ndi atsikana za Yesu.

Timoteo anakondwera kuti Paulo anali bwenzi lake. Iye anakondwera kuti Paulo anamuuza Iye za Yesu. Tsopano Iye anakhozanso kuuza anthu ena za Yesu.



"Bwenzi limakonda nthawi zonse."

(Miyambo 17:17)

PHUNZIRO 3.

PAULO NDI LIDIYA

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Machitidwe 16:13- 15.

MAWU A PAMTIMA:

"Muli abwenzi anga inu..."

Yohane 15:14.

Lidiya ndi abwenzi ake anafuna kupita ku tchalichi. Koma m'mudzi mwaomo munalibe nyumba ya tchalichi. Koterokuti anali kusonkhanira pamphete pa mtsinje.

Lidiya ndi abwenzi ake anakhala panso. Namayimba nyimbo zolemekeza Mulungu. Iwo anali kulankhula ndi Mulungu.

Tsiku lina Lidiya ndi mnezake wina anasonkhana. Iwo anali kukhala m'mphete mwa mtsinje. Iwo anali kuyimba nyimbo za chilemekezo ndi kulankhula ndi Mulungu. Iwo anaona amuna anai akubwera ku mtsinjeko. Lidiya ndi anzake anadabwa kuti, "Kodi amuna amenewa ndi ndani?" Amunawo anasendezera pafupi, posachedwa anafika kumene kunali Lidiya ndi anzake.

Paulo m'modzi wa amunawo anati, "Dzina langa ndine Paulo. Awa ndi athandizi anga, Luka, Sila ndi Timoteo. Iye tayenda ulendo wautali. Tabwera kudzamva za Yesu Mwana wa Mulungu."

Lidiya anauza Paulo ndi abwenzi ake dzina lake. Iye anati, "Tikondwera kuti mwabwera. Kodi Yesu ameneyu ndani? Chonde tatiuzani za Iye." Paulo anati, "Yesu anabadwira m'Betelehemu. Ndipo anakula kukhala mwamuna. Iye anapitapita kunka nachita zabwino. Iye anachiritsa odwala. Iye anapenyetsa akhungu. Kuli konse kumene Iye anapita anathandiza anthu. Yesu anali bwenzi labwino kwa aliyense.

Paulo anauza Lidiya ndi abwenzi ake zinthu zambiri za Yesu.

Paulo pamene Iye analekeza kulankhula. Lidiya anati, "Chonde tatiuzaninso za Yesu."

Paulo anayambanso kulankhula nati, "Yesu amakonda aliyense. Yesu amakukondani inu, Iye ndi bwenzi lanu. Yesu akufuna kuti inu mumkonde Iye. Iye akufuna kuti inunso mukhale abwenzi ake."

Lidiya ndi abwenzi ake anati, "Ife timakonda Yesu. Tikufuna kuti, Iye akhale bwenzi lathu. Ifenso tikhale abwenzi ake. Lidiya ndi abwenzi ake anali osangalala kwambiri. Lidiya anati, "Ife tikufuna kuti inu mukhale m'mudzi mwathu muno. Chonde bwerani mudzakhale kunyumba kwanga." Paulo ndi athandizi ake anakhala kunyumba kwa Lidiya. Anthu ambiri anadza kudzamva Paulo akuwaphunzitsa za Yesu. Lidiya anakondwera kuti iye anakomana ndi Paulo ndi abwenzi ake.



"...Ndiani abwenzi anga." (Yohane 13:14)

SAMUELI ATHANDIZA

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: 1 Samueli 1- 3.

MAWU A PAMTIMA:

"... Tikhala othandizana ..."

(2 Akorinto 1:24)

Samueli anautsidwa m'mamawa. Iye anadyetsa ziweto. Iye anadya chakudya chake cha m'mawa. Pamenepo anavala malaya ake atsopano.

Lero ndi tsiku lapadera. Samueli anali wokondwa kwambiri. Lero Samueli anali kupita ku tchalichi cha ku Silo.

Mai ake Hana anamuitana iye nati, "Samueli, kodi wakonzeka? Tikhoza kupita tsopano." Samueli anayankha kuti, "Inde ndakonzeka."

Samueli, Elikana ndi Hana anayamba ulendo wawo mu mseu. Unali ulendo wautali kupita ku tchalichi cha ku Silo.

M'mene Samueli anali kuyenda, anali kuganiza za tchalichi, kuti "Kodi ndilotani? Nanga Mlaliki ndi munthu wotani?" Samueli anaganiza zimene iye angachite pofuna kuthandiza mlaliki.

Samueli anafunsa mai wake kuti, "Kodi tchalichilo ndi lotani?" Hana anati, "Ndi malo okongola kwambiri, liri ndi makatani ofiira ndi nyale za golide." Samueli anafunsanso kuti, "Nanga dzina la Maliki ndi ndani?" Elikana anati, "Dzina lake ndi Eli. Iye ndi munthu wokalamba, ndipo ndi munthu wabwino kwambiri. udzamkonda kwambiri mlaliki Eli."

Samueli, Hana ndi Elikana anayenda nthawi yaitali. Pomaliza anafika ku tchalichi.

Samueli, Hana ndi Elikana analowa m'tchalichi. Samueli anaona munthu wokoma mtima ndi wachimwemwe chabwino.


Hana anati, "Mlaliki Eli, uyu ndi mwana wanga Samueli."

Ameneyu amandithandiza kunyumba kwathu. Iye akufunanso kuthandiza ku tchalichi kuno."

Mlaliki anasekerera Samueli. Iye anagwira dzanja la Samueli ndi dzimanja dzake dziwiri nati, "Samueli ndakondwera kuti wabwera. Iwe ukhoza kundithandiza kuchita zinthu zambiri." Samueli anafunsa kuti, "Ndikhoza kuchita chiyani?"

Mlaliki Eli anaunguzaunguza. Iye anaona mipando yokongola ya matabwa. Ndipo anauza Samueli kuti, "Ndikufuna wina wondithandiza kupukuta mipandoyi." Iye anaonanso choikapo nyali cha mkuwa nati, "Mupukutenso nyalizi. Ndiponso mudzadzemo mafuta."

Samueli anasekerera mlaliki Eli nati, "Ndikhoza kuchita zimenezi." Eli anati, "Samueli ndaona kuti mukhala mthandizi wabwino." Ndipo Samueli anali mthandizi wabwino.



"....Tikhala othandizana..." (2 Akorano 1:1)

PHUNZIRO 5.

YESU APHUNZITSA ZA CHISAMALIRO CHA MULUNGU

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Mateyu 6:25- 34.

MAWU A PAMTIMA:

"Mulungu...asamalira inu..."

(1 Petro 5:6,7)

Yesu anakhala pa thanthwe lalikulu pambali pa phiri. Anthu ambiri anamzungulira Iye. Ena anaima ambiri pambali pake. Anthuwo anadza kudzamva Yesu akunena za Mulungu. Amai ndi Abambo anasonkhana. Anyamata ndi atsikana anadza. Ena aiwo anayenda kuchokera kutali. Aliyense anamvetsera mwa chete m, mene Yesu anali kulankhula.

Yesu anati, "Mulungu amakukondani inu kwambiri, Mulungu anandituma ine kuti ndidzakuuzeni kuti Iye amakukondani. Iye akufuna kuti inu mudziwe kuti Iye amakusamalirani. Iye amafuna kuti inu mukhale okondwa."

Yesu anayang'ana amai ndi abambo nati, "Musadere nkhawa za chimene mudzadya. Musadere nkhawa kuti madzi akumwa tidzawatenga kuti. Musadere nkhawa za chovala."

Yesu anayang'ana kumwamba. Iye anaona mbalame zikuuluka pamwamba. Anthu onse anayang'ananso naona mbalame. Yesu anati, "Mvetsetsani mbalame zikuimbazo. Mulungu amazisamalira zimenezo. Iye amazipatsa izo chakudya koma inu ndinu ofunika kwambiri kwa Mulungu kuposa mbalame. Mulungu amakusamalirani."

Yesu anayang'ana maluwa amene anamera pa phiri. Iye anaona maluwa ofiira ndi achikasu. Iye anaona maluwa ang'ono ndi akulu. Iye anaona maluwa atali ndi aafupi. Yesu anati, "Maluwa awa ndi okongola kwambiri. Mulungu amawasamalira. Iye amawakulitsa.

Iye amawakongoletsa. Koma inu ndinu ofunika koposa pamaso pa Mulungu kuposa maluwawa. Mulungu amakusamalirani."

Yesu anaima. Iye anayang'ana amai ndi abambo onse. Iye anayang'ananso anyamata ndi atsikana. Ndipo anati, "Mulungu amadziwa kuti mumasowa chakudya. Mulungu amadziwa kuti mumasowa madzi akumwa. Iye amadziwa kuti mumasowa chovala. Koma musadere nkhwaza za zinthu zimenezi. Ingophunzirani kuchita zinthu zimene zingakondweretse Mulungu. Phunzirani kuchita zinthu zimene Mulungu akufuna kuti inu muchite."

Amai ndi abambo anali okondwera kwambiri. Anyamata ndi atsikana anali okondweranso. Iwo anadziwa kuti Mulungu amawakonda iwo. Iwo anadziwa kuti Mulungu amawasamalira. Yesu anawauza kotero.



"Muligu...amakusamalirani..." (1 Petro 5:6-7)

PHUNZIRO 6.

ULENDO WA YAKOBO

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Genesis 28.

MAWU A PAMTIMA:

"...Mulungu... Muika mdima ndipo pali
usiku..." (Masalmo 104:1,20)

Isaki anaitana mwana wake nati, "Yakobo, Yakobo ndikufuna kuti upite pa ulendo wautali. Ndikufuna kuti ukacheze kwa malume wako Labani."

Malume Labani amakhala kutali kwabasi. Mai wake anamkonzera kamba wapanjira. Mayi ake pamodzi ndi Isaki anatsazikana naye. Iwo anapempha Mulungu kuti asamalire mwana wawo.

Yakobo anayamba ulendo wake wautali. Iye anayenda kupita kwawo kwa malume Labani. Dzuwa linali kumutentha pa msana. Mphepo ya yaziyazi inali kuombera nkhope yake. Iye anaona mitengo yokongola mnjira monse.

Posachedwa Yakobo anatopa ndi njala ija anapumula pang'ono. Pamenepo anadya chakudya chimene amai ake anamukonzera.

Yakobo anayenda nthawi yaitali. Mphepo inayamba kuzizira. Dzuwa linali kulowa. Mdimba unayandikira. Pamenepo Yakobo anayamba kuona nyenyezi imodziimodzi. Pomaliza kunamdera. Yakobo anaima. Ndipo anayamba kuganiza kuti, "Koma ndigone pompano." Iye anaunguzaunguza, naona malo abwino oyenera kugona. Iye anapeza mwala wabwino wotsamira. Yakobo anadzizinga ndi mkanjo wake kuti afundidwe. Iye anagona mwa phee ndi kuyang'ana mitamobo yakongola. Iye anamvetsera phokoso la usiku. Kapena anali kuganiza kwawo naona ngati watayika.

Posachedwa Yakobo anagona tulo. Atagona analota atulo. Ali mutulo Mulungu analankhula ndi Yakobo nati, "Yakobo, ndiri nawe pano. Ndidzakhala nawebe nthawi zonse. Ndidzakusamalira iwe.

Ndidzakusamalira kuli konse kumene upitako."

Yakobo anauka. Iye anakhala tsonga naunguzunguza. Iye sanaona aliyense. Iye anangoona nyenyezi ndi m'mitambo. Iye sanamvenso mawu alionse. Iye anangomva phokoso la usiku.

Yakobo anati, "Tsopano Mulungu ali ndi ine. Iye adzakhala nane kulikonse kumene ndipita, ndisakhalenso osaukidwa. Sindiyeneranso kuchita mantha. Mulungu adzandisamalira ine."



"...Mulungu...Muika mdima ndipo pali nsiku..."
(Masalmo 104:1,20)

MAFUNDE AKULU

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Marko 4:35- 41.

MAWU A PAMTIMA:

"...Inu muli pafupi Yehova..."

(Masalmo 119:151)

Yesu anali wotopa. Iye anafuna kupumula. Iye anakhala akuphunzitsa anthu tsiku lonse. Tsopano kunali madzulo.

Iye anati kwa abwenzi ake, "Tiyeni tipite patsidya pa nyanja." Abwenzi a Yesu anali okondwera kuti anali ndi ngalawa. Iwo anakhoza kuolotsa Yesu. Iwo anakankhira bwato m'madzi ndipo anaika mathanga awo.

Yesu analowa m'bwato. Iye anakhala pansi kumbuyo. Iye anatsamira mutu wake pa mtsamiro. Kunalibe mphepo yoyendetsa mathanga. Koterok anthuwo anakankhira bwato m'madzimo. Mkamphindi kochepa Yesu anagona tulo.

Posachedwa mphepo yozizira inayamba kuomba bwato linayamba kukanthika. Mtambo wochindikira wakuda unabisa timitambo. Mitambo inabisa mwezi ndi nyenyezi. Kunali mdima waukulu.

Mphepo inakula ndipo mafunde anagavila m'bwato. Mafunde anakula bwato liyamba kulowa madzi.

Abwenzi a Yesu anayesa kutembenuza bwato kuloza kudooko koma mphepo inawabweza. Anthu anachita mantha ngakhale anakhala akuona mafunde kale. Koma sanaone mafunde ofanana ndi amenewa.

Madzi anayamba kulowa m'bwato. Anthuwa anadziwa kuti posachedwa madzi adzadza m'bwato.

Iwo anayamba kufuula kuti, "Yesu ali kuti?" Koma Yesu analikugona pambuyo pa bwato. Iye anali tulobe. Phokoso la mphepo ndi mafunde sizinamuutse Iye.

Abwenzi a Yesu anafuula mwa mantha nati,

"Yesu, Yesu, bwato likudzadza ndi madzi ndipo posachedwa limira."

Yesu anatsegula maso ake. Iye anaona kuti m'bwato mwalowa madzi. Iya anaombedwa ndi mphepo yozizira pankhope pake. Mwamsanga Yesu anaimilira m'bwato lovutikalo. Iye anatambasula manja ake. Pompo Iye anati, "Khala bata."

Posachedwa mphepo inaleka kuomba. Madzi anakhala bata. Bwato linaleka kuyandama. Mwezi ndi nyenyezi zinawalanso. Mitambo inapita. Mafunde anatha.

Abwenzi a Yesu analibenso mantha. Iwo anadziwa kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Iye adzawasamalira iwo nthawi zonse. Iye adzakhala nawo pafupi nthawi zonse.



"...Inu muli pafupi Yehova..." (Masalmo 119:151)

PHUNZIRO 8.

MMENE KAZEMBE NAMANI AMADWALA

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: 2 Mafumu 5:1- 19.

MAWU A PAMTIMA:

"...Yehova ndiye wabwino..."

(Masalmo 34:8)

Kazembe Namani anali mtsogoleri wa khamu lalikulu la ankhondo. Kale anali munthu wamphamvu. Koma tsopano anali kudwala. Iye anali ndi zironda mmanja mwake. Iye anali ndi zironda m'mikono ndi mmiyendo. Iye anali ndi zironda thupi lake lonse.

M'nyumba mwa Namani munali kukhala kabuthu kena kantchito. Iko kamathandiza mkazi wa Namani. Iko kanaona kuti nkhope ya mkazi wa Namani inali ya chisoni. Mtsikanayo anati, "Bwanji mai muli ndi chisoni? Mukuliranjiji?"

Mkazi wa Namani anati, "Mwamuna wanga akudwala, sing'anga sangathe kumchiritisa." Mtsikanayo anati, "Mulungu akhoza kuwachiritisa. Kunali kwabwino ngwazi Namani akadapita kukaonana ndi Mlaliki Elisa. Iye amakhala ku Samariya. Iyeyu adzapempha Mulungu kuti achiritse ngwazi Namani."

Mkazi wa Namani anathamangira kwa mwamuna wake. Iye anauza Namani zimene ananena mtsikanayo. Namani anati, "Ndidzapita ku Samariya. Ndipita ndikamuone Elisa. Kapena Mulungu wake akhoza kundithanidza ine."

Ngwazi Namani anauza anyamata ake kubweretsa akavalo. Iye anawatuma iwo kuti akatenge gareta. Mosachedwa iwo anayamba ulendo wao wa ku Samariya. Elisa anamva kuti Namani wabwera ku Samariya. Iye anamva kuti Namani anali munthu wodwala kwambiri. Elisa anatumiza amithenga kuti akauze Namani chimene adayenera kuchita, nati, "Pitani mukauze Namani kuti apite kumtsinje wa Yorodano."

Mukamuuze iye akasambe mumtsinjemo kasanu ndi kawiri. Pamenepo Mulungu adzamumchiritsa."

M'thenga unapita kwa Namani. Namuuzza iye zimene Elisa wanena kuti iye achite.

Koma Namani anati, "Ai, sindigakasambe mmadzi amatope aja. Tiyeni tizipita kwathu." Ulendo obwerera. Posachedwa iwo anafika kumtsinje wa Yordano.

M'modzi wa athandizi anaimitsa gareta nati kwa ngwazi Namani, "Mlaliki Elisa anakuuzani inu m'mene mungachirire. Chimene chiri chinthu chapafupi kuchita, kuti mungosamba mumtsinje kasanu ndi kawiri basi."

Ngwazi Namani anatsika pa gareta wake. Iye anatsikira m'madzi. Iye anasamba koyamba, kachiwiri, kachitatu mpaka kasanu ndi kamodzi ndipo mmene iye anasamba kachisanu ndi kawiri, zironda zake zonse zinatha. Khungu lake linakonzekanso. Mulungu anachiza ngwazi Namani.



"...Yehova ndiye wabwino.." (Masalmo 34:8)

PHUNZIRO 9.

CHAKUDYA CHABWINO CHA DANIELI

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Danieli 1.

MAWU A PAMTIMA:

"Ndipo mwanayo anakula..."

Luka 2:40

Mfumu ya ku Babulo inafuna athandizi apadera. Iyo inafuna athandizi amphamvu. Iyo inafuna athandizi anzeru.

Tsiku lina Mfumu inaitana mnyamata wake wamkuru, nimuza kuti, "Pita ukasankhe anyamata abwino a m'dziko mwanga muno. Ubwere nawo kuti adzakhale kunyumba ya Mfumu. Uwaphunzitse kunditumikira. Uwadyetse chakudya chabwino ndi vinyo. Ndikufuna kuti athandizi anga akhale athanzi ndi amphamvu.

Mnyamata wotchedwa Danieli anasankhidwa kukatumikira mfumu. Atatu a anzake a Danieli anasankhidwanso. Iwo anapita kukakhala ku chinyumba cha mfumu.

Pa nthawi ya chakudya, anyamata a Mfumu anawabweretsera chakudya anyamatawo. Danieli anakhala pa chakudya ndi abwenzi ake. Iye anayang'ana chakudya chabwinocho, anayang'ananso vinyoyo.

Danieli anaitana mnyamata wa mfumu nati, "Ife sitikhoza kudya chakudya chimenechi. Chakudya choterechi ndi vinyoyu sichabwino kwa anyamata. Chonde simugathe kutipatsa ndiwo zokha? Ndi kuti tidzimwa madzi okha?"

Mnyamatayo anadandaula nati, "Mfumu inandiuza ine kukupatsani chakudya chabwino. Anandiuzanso kuti ndizikupatsani vinyo. Iye akufuna kuti inu mukhale ndi mphamvu. Muyenera kudya chakudya ndi kumwera vinyoyu. Ngati mutakana mfumu idzapsya mtima."


Danieli anaganiza mkamphindi, nafunsa kuti,

"Simungathe kuyamba mwatipatsa chakudya china poyamba? Tayambani mwatipatsa ndiwo zokha ndi madzi akumwa kwa masiku khumi." Anyamata enawa atayamba adya chakudya cha mfumuchi ndi kumwera vinyo. Pamenepo muoneno kuti ndani ati akhale wamphamvu." Anatero Danieli.

Mnyamata wa mfumu anati kwa Danieli.

"Imeneyo ndi nzeru yabwino." Tsiku ndi tsiku Danieli ndi abwenzi ake anadya ndiwo zokha, ndi kumwa madzi okha. Anyamata ena anadya chakudya chabwino ndi kumwera vinyo.

Patatha masiku khumi, Danieli ndi anzake anadzionetsera kwa mnyamata wa mfumu. Anyamata ena onse anaima nawo pamodzi. Mnyamata wa mfumu anayang'ana anyamata onsewo. Pamenepo analankhula kwa Danieli nati, "Iwe ndi abwenzi akowa mukuoneka athanzi labwino. Inu ndinu amphamvu kuposa anzanuwa. Matupi anu ndi osalala ndi ooneka bwino. Maso anunso ndi akucha ndi abwino. Mumanena zooni. Ndiwo ndi madzi ndizo chakudya chabwino chothandiza anyamata kukula bwino. Inu mudzakhala athandizi abwino a mfumu.



"Ndipo mwanayo anakula..." (Luka 2:40).

MMENE KHOMA LINAMANGIDWIRA

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Nehemiya 1:1- 6:16.

MAWU A PAMTIMA:

"...Gwirani ntchito ndi manja anu..."

(1 Atesalonika 4:11)

Tsiku lina bwenzi linafika kudzaona Nehemiya. Iye anali wa chisoni kwambiri. Ndipo bwenzilo linafunsa Nehemiya kuti, "Kodi mumakumbukira mbiri ya mzinda wa Yerusalemu. Mzindawu unali wozingidwa ndi khoma lalikulu. Ndipo khomalo linali ndi zipata zazikuluzikulu zimene zinali kutsekedwa. Koterokuti adani sanali kukwanitsa kulowa mu mzindamo."

Nehemiya anati, "Inde ndikukumbuka." Bwenzi lake linati, "Koma tsopano zipata zidaonongeka. Khoma lidagumuka adani akumangolowa usiku uliwonse."

Nehemiya anali ndi chisoni kwambiri. Iye anapemphera kuti Mulungu amthandize. Tsiku lina Nehemiya anali ndi Mfumu. Ndipo Mfumu inamfunsa kuti, "Bwanji mukuoneka wachisoni Nehemiya, mwatani?" Nehemiya anati, "Malinga a Yerusalemu agumuka zipata zathyokathyoka. Sindimafuna kuti zinthu zotere zioneke mu Yerusalemu."

Mfumu inafunsa Nehemiya kuti, "Nanga umafuna kuti uchite chiyani?" Yeremiya anati, "Ndimafuna ndipite ku Yerusalemu kuti ndikakonze malinga ndi zipata zake. Ndipo ndi mafunanso ndalama kuti ndikagule miyala." Mfumu inati, "Chabwino ndikupatsa ndalama. Koma sungathe kumanga malinga iwe wekha." Nehemiya anati, "Ndidzapezanso anthu ena ondithandiza kumanga malinga."


Nehemiya anathamangira ku Yerusalemu. Iye anaona malinga ogumuka, Iye anaona kuti zipata zinaonongeka. Nehemiya anafunsa kuti, "Ndani angandithandize kukonza malinga?"

Abambo ena anati, "Ife tidzakuthandizani." Amai ena anatinso, "Ife tidzakuthandizani."

Posachedwa anthu anayamba kukonza malinga ndi zipata. Iwo ananyamula miyala yolemera. Iwo anaika umodzi pamwamba pa unzake. Nthawi zina anthuwo anali wotopa, anafuna kuleka, koma Nehemiya anawapempha iwo kuti agwirebe ntchito. Nehemiya anati, "Ena a ife akaleka sitikwanitsa kumaliza ntchitoyi. Tiyenera kugwirabe ntchito ngakhale titatopa."

Anthu anagwira ntchito kwa masiku khumi, anagwira ntchito makumi awiri. Iwo anagwira makumi atatu. Anai, mpaka makumi asanu. Iwo anagwira ntchito masiku makumi asanu ndi awiri mpaka anamaliza yonse. Anthu anaona zipata. Iwo anaona malinga. Iwo anakondwera kuti khoma linalinso lamphamvu. Anthu anakondwera kuti anagwira ntchito kolimba.

Nehemiya anauza abwenzi ake kuti, zikomo mwandithandiza, takonza khomali chifukwa aliyense amathangata."



"...Gwirani atchito ndi manja anu..."

(1 Atesalonika 4:11)

PHOSO LA MNYAMATA

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Mateyu 14:15- 21;
Yohane 6:1- 13.

MAWU A PAMTIMA:

"...Tikondane wina ndi mnzake..."

(1 Yohane 4:7)

Mnyamata anali kuyenda mumsewu. Atagwiritsitsa dengu m'manja mwake. Iye sanafune kutaya phoso lake.

Posachedwa mnyamata anaona chikhamu cha anthu. Iye anaona amai ndi abambo. Iye anaonanso anyamata ndi atsikana. Iwo onse anali kumvetsera kwa Yesu. Yesu anali kuwauza iwo za chikondi cha Mulungu.

Mnyamatayo analowerera nao m'khamumo. Iye anaona Yesu atakhala pa thanthwe lalikulu. Mnyamatayo anakhala pa msipu. Iye anamvetsera ludzu lokoma mtima. Aliyense anamvetsera Yesu alikulankhula.

M'mene Yesu anatha kulankhula, dzuwa linali pafupi kulowa. Mwadzidzidzi mnyamatayo anamva njala. Iye anakumbukira nsomba ndi mkate zimene zinali m'dengu mwake. Iye anavundukula mdengu naturutsa chakudyacho.

Pompo amamva Yesu akulankhula ndi mthandizi wake Filipo. Yesu anati, "Anthuwa ali ndi njala. Sitingathe kuwachotsa chomwechi osadya. Tiyenera kuwapatsa kanthu kena kuti adye."

Filipi anayankha kuti, "Sitingathe kugula chakudya chokwanira anthu onsewa." Pano pali anthu ambiri.

Mnyamata anaganiza za phoso lake. Iye anathamangira kwa Andrey, m'modzi wa athandizi a Yesu, anati, "Ndikhoza kukupatsani mkate ndi nsomba zanga."

Andrey anasekerera. Iye anatenga phoso la mnyamatalo.

Iye anawerenga naona kuti ndi timikate tisanu ndi nsomba ziwiri.

Andreya anapita kwa Yesu nati, "Siuyu mnyamata ali ndi chakudya. Iye ali ndi timikate ndi nsomba. Komanso sizokwanira kudyetsa anthu onsewa."

Yesu anati, "Chonde auze anthuwa akhale pansi." Anthu anakhala pansi pa msipu. Pompo Yesu anatenga phoso lija. Iye anapemphera nati, "Zikomo Mulungu chifukwa cha mkate ndi nsomba." Yesu anagawa mkate ndi nsomba. Iye anauza ophunzira ake kuti apatse aliyense chakudyachi. "Muwauze kuti adye monga momwe angathere." Anatero Yesu.

Aliyense anadya chakudya monga mwa njala yake. Pompo athandizi a Yesu anatola makombo.

Mnyamatayo anathamangira kwao, ndipo anali wosangalala kwambiri. Chifukwa anagawira Yesu phoso lake.



"...Tikondane wina ndi mnzake.." (1 Yohane 4:7)

PHUNZIRO 12.

DAVIDE NDI MUNTHU WOPUNDUKA

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: 2 Samueli 9.

MAWU A PAMTIMA:

*"...Mukhalirane okoma wina ndi mnzake."
(Aefeso 4:32)*

Tsiku lina mfumu Davide anakhala mnyumba yake ya chifumu. Mfumu Davide anali kuganiza.

Iye anakumbukira m'mene iye anali mnyamata. Iye anakumbukira bwenzi lake Jonatani. Iye anakumbukira m'mene iye ndi Jonatani anasewerera limodzi. Iye anakumbukira nkhani zimene anali kukambirana.

Mfumu Davide anayang'ana mkondo umene Jonatani anapatsa. Iye anayang'ana lamba amene Jonatani anampatsa. Iye anakumbukira m'mene anapangirana kuti adzakhala abwenzi nthawi zonse.

Mfumu Davide anaitana ena mwa athandizi ake nawafunsa kuti, "Kodi mbumba ya Jonatani ndingaipeze kuti, ndinafuno ndidakawachitira za chifundo zina."

M'modzi wa athandizi ake anati, "Ndimadziwa m'modzi wa anyamata a Jonatani, Ziba. Ameneyo ndiye angakuuzeni za mbumba ya Jonatani."

Davide anati, "M'bweretseni kuno." Mthandiziyo anafulumira kunka nafuna Ziba. Iye anauza Ziba kuti mfumu ikufuna kumuona. Ziba anadza mofulumira.

Davide anamfunsa kuti, "Monga pali wina amene anatsala mbanja la Jonatani." Ziba anati, "Inde Jonatani anali ndi mwana wa mwamuna. Iye anapweteka akali mwana. Tsopano ndi wopunduka mapazi onse awiri. Dzina lake ndi Mefiboseti."

Davide anafunsa kuti, "Nanga akukhala kuti?" Ziba ananena kuti, "Mwana wa Jonatani alibe nyumba yakeyake. Iye akukhala kunyumba ya bwenzi lake."

Davide anati, "M'bweretseni kuno kwa ine Mefiboseti, ndikufuna kumchitira zachifundo zina."

Ziba anapita kukapeza Mefiboseti ndi banja lake. Iye anabwera nawo kuti adzaonane ndi Mfumu Davide, iye anagwada pamapazi ake. Mfumu Davide anyang'ana pa munthu wopundukayo nati Mfumu Davide, "Usaope, Atate ako ndi ine panali ubwenzi waukulu. Iye anandichitira zinthu zambiri. Ine ndikufuna kukhala bwenzi lako. Ndikufuna kukuchitira zachifundo."

Mefiboseti anayang'ana Mfumu Davide. Iye analibenso mantha.

Davide anati, "Bwera udzakhale ndi ine kunyumba yanga ya Chifumu. Ukabwere ndi banja lako lomwe tsiku ndi tsiku ndikufuna kuti udzidya pa gome langa."

Mefiboseti anati, "Zikomo Mfumu Davide, ndakondwera kuti inu ndinu bwenzi langa. Ndakondwera kuti mwandikomera mtima kotere."



"...Mukhalirane okoma wina ndi mnzake."

{Aefeso 4:32}

PHUNZIRO 13.

MSAMARIYA WACHIFUNDO

MAWU OWERENGA KUNYUMBA: Luka 10:30- 37.

MAWU A PAMTIMA:

"...ndidzakuthangata..."

(Yesaya 41:10)

Nthawi zina Yesu anali kunena mafanizo kuthandiza anthu kuti adziwe chakuti achite.

Tsiku lina munthu wina anafunsa Yesu funso. Yesu ananena nkhani iyi kuthandiza munthu uja kuti amvetsetse bwino.

Munthu wina anali kuchokera ku Yerusalemu ndipo anali kupita ku Yeriko. Anthu akuba anamuimitsa. Anamubera ndi kumuvulaza ndipo anamusiya m'mbali mwa msewu ali chigonere.

Munthu uja ali chigonere choncho anamva munthu wina ali kubwera. Munthuyo anafika koma sanaime anadzera mbali ina ya msewu. Munthu uja anaima ndipo anamuyang'ana munthu wovulala uja ndipo anapita ndi kumusiya. Munthu wovulala uja anamvanso munthu wina ali kubwera ndipo nthawi imeneyi anali munthu wina atakwera buru. Buru uja anafika pafupi. Tsono munthu wovulala uja anamuyang'ana. Anaona munthu uja ali kutsika pa buru wake uja. Munthu ameneyu anali kutsika kuti amuthandize. Munthu wachifundoyu anali kuchokera ku Samariya. A Samariya nawonso samagwirizana ndi mtundu wa munthu amene anavulalayu.

Munthu wa ku Samariya uja anamuona munthuyu. Anati, "Ndikuthandiza." Anampaka mankhwala m'zirona monse muja. "Ndikakuika ku malo abwino. Ukhoza kukhala kumeneko usiku wonse."

Munthuyo anamuimiritsa munthu wovulala uja mosamala bwino. Anamukweza pa buru wake uja ndi kupita naye ku nyumba yogona alendo.

Munthu wa chifundoyo analowa naye m'nyumba
yogona alendo munthu wovulalayo. Anamusamalira
usiku wonse. M'mawa mwake munthu wachifundo
uja anamupatsa ndalama munthu wosamalira nyumba
ya alendo uja ndipo anamuuza kuti amusamaliire
munthuyo pamene iye achoke. Msamariya uja anali
bwenzi labwino kwa munthu wovulala uja. Mulungu
ali kufuna kuti ifenso tikhale othandiza.



"..Ndizakuthangata.." (Yesaya 41:10)